# Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

**Za kulengedwa kwa zonse ndi kucimwa koyamba**

1. Mulungu analenga zonse bwino
2. Mulungu anatilenga bwino
3. Mulungu analenga zonse kuti atamandidwe
4. Momwe chimo linabwera pa dziko lapansi
5. Zimene zinacitika kwa Adamu ndi Hava
6. Citanthauzo ca kukhala wocimwa
7. Zifukwa zake za kulangidwa kwa uchimo

Zolembedwa zina za m'bukuli zinasandulidwa kucokera mu buku la 'Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.'

© Stephanos Zambia Trust
www.kudzidwazamulungu.com

# 1. Mulungu analenga zonse bwino

*Paciyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi - Genesis 1.1*

**Kuwerenga**
Genesis 1.20-25

**Malongosoledwe**
Kodi mwaona cinthu codabwitsa kwambiri lero?
Kuli zinthu zambiri zodabwitsa kwambiri. Zinthu zodabwitsa ziri pafupi ndi ife. Dziko lonse lapansi lalikulu ndilo lodabwitsa. Thambo waukulu wobiriwira m'mwamba ndiwo wodabwitsa.
Nthawi zina tiona mitambo yoyera yoyenda m'thambo monga mabwato okongola. Mitambo ndiyonso yodabwitsa. Mitambo ndiyo zipompho zing'ono-zing'ono za madzi zoombedwa ndi mphepo. Usiku kuli nyenyezi zokongola zimene zimaunikira m'thambo. Kuli nyenyezi zambiri-mbiri!
Kuli maluwa okongola ndi mitengo yokongola. Kuli agulugufe okongola. Kuli mitundu yambiri ya miswe imene imapanga zulu ndiponso mitundu ya nyerere imene ipanga nyumba zao m'munsi m'dziko. Kuli nyama zaubweya zokhala m'nkhalango. Kuli akalulu ndi agologolo. Kuli mbalame zoimba ndi zouluka zimene zimapanga mafukwe odabwitsa.
Ooo, dziko lapansi ndi malo odabwitsa!
Kodi dziko lapansi ndi zodabwitsa zonse zinacokera kuti?
Tidziwa kumene zinacokera. Taphunzira m'Baibulo kuti Mulungu analenga zonse. Anazilenga kale kale: paciyambi.
Kusanakhale nthawi ya ciyambi, kale kale kwambiri, kunalibe thambo. Kunalibe dziko lapansi lalikulu. Kunalibe mitambo, mitengo, mbalame ndi maluwa. Kunalibe anthu.
Koma Mulungu analiko. Iye ndiye *INE NDINE YEMWE NDIRI INE* (Eksodo 3.14). Iye akhala Kumwamba: m'mwamba mwa thambo. Mulungu analiko nthawi zonse. Ndipo tsiku lina anayamba kulenga zabwino zodabwitsa zimene timaona.
Poyamba Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi. Kumwamba ndi thambo ndipo dziko lapansi ndi kunja kuno.
Koma kumwamba kunali mdima. Ku dziko lonse lapansi kunalinso mdima.
Kenaka Mulungu anati, 'Kuyere'. Ndipo kunayera.
Mulungu ndiye Kuunika. Analenga kuunika ku dziko lapansi kuti tingamdziwe ndiponso kuti tingaone zolengedwa zace ndi kusangalatsa nazo.
Analenga nyanja yaikulu, nyanja yaing'ono ndi mitsinje. Anatuma madzi ena ku thambo kuti kuli mitambo.
Anapanga mapiri ndi mapiri ang'ono. Analenga mitengo, udzu ndi maluwa. Analenga timbalame ndi njobvu zazikulu. Analankhula mau ndipo kunacitika!
Ndipo zonse zimene Mulungu analenga zinali zabwino kwambiri. Mulungu ndiye wamkulu kwambiri!

**Kukambirana**
1. Kodi tidziwa bwanji kuti Mulungu analenga zonse?
2. Kodi Mulungu analenga zonse mogwiritsa nchito ciani?
3. Kodi tingasamalire bwanji cilengedwe ca Mulungu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Tikuyamikani kuti munalenga zonse zabwino ndi zokongola. Sitimvetsa njira imene maluwa amamwa madzi. Sitimvetsa njira imene mitengo imabala zipatso. Sitimvetsa njira imene mitambo imayenda m'thambo. Koma mumvetsa zonse cifukwa Inu ndinu Mlengi wa zonse. Ndinu wamphamvu kwambiri. Mutiphunzitse kukhala miyoyo ywathu ku ulemerero wanu. M'dzina la Yesu Kristu tikupemphani izi. Amen.

# 2. Mulungu anatilenga bwino

*Mulungu ndipo adalenga munthu m'cifanizo cace – Genesis 1.27a*

**Kuwerenga**

Genesis 1.26-28, Genesis 2.7 ndi 8

**Malongosoledwe**

Kuli anthu ambiri-mbiri pa dziko lapansi. Kuli amuna ndi akazi, anyamata ndi atsikana. Kuli mitundu yambiri. Kodi iwo acokera kuti?

Mulungu analenga iwo onse.

Kale kale Mulungu atalenga dziko lokongola Iye analenga munthu m'modzi. Analenga munthuyo kucokera m'dothi. Anampatsa thupi lokongola ndi manja ndi miyendo. Anampatsa mutu wokongola ndi maso, makutu, pakamwa ndi mpuno. Anampatsa mtima umene umagunda ndiponso nzeru kuti munthu aziganiza. Kenaka Mulungu anauzira mphweya m'mphuno mwace kumpangitsa munthu wamoyo. Mulungu anampatsa mzimu umene sudzafa. Ndiye anapanga munthu mu cifanizo cace. Munthu anali wosiyana ndi nyama.

Mulungu anacha dzina la munthuyo 'Adamu'.

Mulungu anapanganso mkazi m'modzi. Mulungu anamgonetsa Adamu. Pamene Adamu anali m'tulo, Mulungu anacotsa nthiti ya Adamu napanga mkazi mogwiritsa nchito nthitiyo.

Pamene Adamu anauka, Mulungu anampatsa buthuyo wokongola kukhala mkazi wace. Adamu anampatsa dzina. Anamucha Hava. Adamu anakonda Hava. Kotero kunali anthu awiri okondwera pa dziko lapansi, anthu opanda chimo lirilonse. Anakhala m'munda wokongola, ndi mitengo, maluwa ndi nyama. Zonse zinali zodabwitsa ndi zabwino kwambiri.

Mulungu analenga Adamu ndi Hava kuti akhale ndi ana. Anafuna kuti akhale ndi ana. Anafuna kuti dziko lapansi lidzale ndi anthu kuti iwo azimkonda ndi kulemekeza Iye.

Patapita nthawi Adamu ndi Hava anakhala ndi ana. Mwana wobadwa woyamba anali mwamuna. Adamu ndi Hava anali okondwera ndi mwana wao wosangalatsa. Anamucha dzina lace Kaini.

Adamu ndi Hava anakhala ndi ana ena ambiri: amuna ndi akazi.

Ana amuna ndi akazi anakula. Iwo anakwatirana nakhala ndi ana. Pamenepo kunakhala anthu ambiri pa dziko lapansi.

Nthawi zonse Mulungu amalenga ana akhanda onse amene abadwa. Anthu onse amene ali pa dziko lapansi pano ndiwo ana a Adamu ndi Hava.

Adamu anali tate wathu woyamba; Hava anali mai wathu woyamba.

Tidziwa zonsezi cifukwa Baibulo litiuza tero.

Anthu ndi opambana m'zilengedwe zonse zimene Mulungu anapanga, cifukwa Mulungu anapanga munthu m'cifanizo cace.

Anapatsa anthu nzeru zabwino zophunzira ndi zomvetsetsa zonse za pa dziko lapansi. Anthu anadziwa Mulungu. Mulungu anapanga anthu oyamba olungama, kuti kunalibe macimo m'mitima yao. Ndipo Mulungu analenga anthu kuti iwo alamulire zomera ndi nyama. Anapanga anthu kukhala akulu kupambana zolengedwa zonse.

**Kukambirana**

1. Kodi Mulungu analenga Adamu mogwiritsa nchito ciani?
2. Kodi Mulungu anampatsa bwanji Adamu mtima wamoyo?
3. Kodi anthu asiyana ndi nyama n'njira yotani?
4. Mizimu yathu siidzafa. Kodi ici citanthauza ciani?
5. Kutanthauzanji kuti anthu oyamba anali olungama?

**Citsanzo ca pemphero:**

Mulungu Atate Kumwamba, Munatilenga. Cifukwa cace ndife anu. Tikuyamikani, Mlengi wamkulu, cifukwa ca matupi athu olengedwa odabwitsa. Tikhala ndi moyo cifukwa ca Inu. Tikuyamikani kuti munatipatsa mitima ndi nzeru. Conde, mutithandize kukhala miyoyo yathu kwa Inu mwa Yesu Kristu Mpulumutsi. Tikupemphani izi mwa cisomo canu. Amen.

## 3. Mulungu analenga zonse kuti atamandidwe

*Zakumwamba ndi dziko lapansi zimlemekeze – Salimo 69.34a*

**Kuwerenga**
Salimo 150

**Malongosoledwe**
Ndi cifukwa ciani Mulungu anatilenga?
Mulungu sanatilenge cifukwa cakuti Iye anali yekha. Mulungu sali yekha nthawi zonse.
Mulungu anatilenga cifukwa anafuna kutero. Iye anatilenga kuti atamandidwe. Analenga dziko la pansi lokongola kuti anthu akhale komweko; anthu ofanana ndi Iye. Anafuna kuti anthu akhale okondwera ndi kumtamanda Iye cifukwa Iye ndiye wamkulu ndi wolungama kwambiri. Nchito ya Mulungu yolenga zonse inali yodabwitsa. Zonse zimene analenga zinali zokongola ndi zabwino. Zolengedwa zake zonse zinamlemekeza pa ciyambi.
Kodi zonse zinamlemekeza motani Mulungu?
Zolengedwa zonse zinamlemekeza poonetsa ukulu wa Mulungu, ponena za ukulu wake ndiponso pokhala zokondwa ndi zolungama.
Nyenyezi zilemekeza Mulungu pamene ziwala ndi kuunikira m'thambo usiku. Iye azisunga apo. Izo zionetsa momwe ukulu wace uliri.
Dzuwa ndi mwezi zitiuza kuti Iye ndiye Mulungu wa kuunika ndi wa ulemerero, Mulungu wa m'mwamba-mwamba ndi woyera.
Mbalame zimaimba za Iye. Zimatiuza kuti Iye ndi Mulungu wokondwa ndi wacikondwerero.
Mbalame zimaimba za Iye. Zitiuza kuti Mulungu ndiye Mulungu wa cimwemwe ndi cisangalalo. Zimasamalira timbalame tating'ono tao ndipo mwa kucita tero zitionetsa m'mene Mulungu amatisamalira.
Mphepo imaomba molimba ndipo mafunde a nyanja amakhala akulu. Zitiuza kuti Mulungu ndiye wamphamvu ndi wolimba.
Mitengo ndi maluwa, asususu ndi nyerere, nyamalikiti yaikulu ndi mkango wocititsa mantha, mvula yaing'ono ndiponso cipale coyera cofewa – izo zonse zitionetsa kuti Mulungu ndiye wosusumwitsa. Colinga ca kulengedwa kwao ndi kuti zitamandire Mulungu.
Timlemekeza Mulungu titaona zinthu zonse zimene Iye analenga timanena, 'Mulungu ndiye wamkulu ndithu!' Tinganene kwa Iye, 'Ukulu wanu ndi waukulu kwambiri!' Tingamlemekeze bwino kuposa nyama, mbalame ndi nyenezi zimamlemekeza. Tingamdziwe ndi kumkonda. Tiona zonse zolengedwa ndi Iye ndipo mitima yathu iimba, 'Ukulu wanu ndi waukulu kwambiri!'
Timlemekeza Mulungu pamene tiimba nyimbo kwa Iye.
Timlemekeza pamene timyamikira pa zabwino zonse zimene anatilengera ndiponso pamene tikondwera cifukwa ca mphatso zake zabwino.
Timlemekeza pamene tipempha kwa Iye ndiponso pamene timuuza kuti timkonda ndi kumfunika.
Timlemekeza pamene timamvera ndi kuyesa kucita cifuniro cace.
Sitikwaniritsa kumlemekeza mokwanira. Iye ndiye wamkulu ndi wolungama kwambiri.

**Kukambirana**
1. Kodi mbalame zimalemekeza Mulungu m'njira yotani?
2. Kodi maluwa amamlemekeza motani?
3. Ndi cifukwa ciani tingamlemekeza kopambana?
4. Kodi mumalemekeza Mulungu m'njira yotani?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwamba, nchito zanu zonse zimaonetsa ukulu wanu. Mbalame zimakulemekezani. Mitengo imakulemekezani. Cilengedwe conse cimakulemekezani potionetsa ukulu wanu. Mutipatse mitima imene imakulemekezani. Mwa Yesu Kristu tikupemphani izi. Amen.

# 4. Momwe chimo linabwera pa dziko lapansi

*Ndipo chimo ndilo kusayeruzika – 1 Yohane 3.4b*

**Kuwerenga**
Genesis 3.1-6

**Malongosoledwe**
Pamene Mulungu analenga dziko lapansi, analenga zinthu zonse zokongola ndi zabwino koposa! Ndipo anthu oyamba anali okondwera kwambiri! Koma tsopano zambiri siziri zokongola ndi zabwino. Ndipo nthawi zambiri anthu sakondwera. Kuli matenda ndi cisoni; kuli kudana ndi mkwiyo. Kuli anthu odzikonda ndi anthu ocita zoipa. Kuli kuyambana ndi kumenyana.
Ndi ciani ciri kucitika? Ndi ciani cimene cinacitika kwa dziko lapansi lokongola ndi kwa anthu amene anakondwera pa ciyambi?
Chimo linabwera. Chimo linaononga dziko lapansi lokongola la Mulungu.
Kodi chimo linalowa bwanji m'cilengedwe cokongola ca Mulungu? Baibulo litiuza momwe ico cinacitika.
Mulungu ali ndi mdani, mdani wamkulu: Satana. Satana ndiye mngelo woipa. Akuda Mulungu. Ndipo afuna kuti aliyense azida Mulungu. Ndipo amanena mabodza, ngakhale mabodza a Mulungu.
Satana anayang'anira Mulungu polenga dziko lapansi lokongola ndi thambo la kumwamba. Anayang'ana Mulungu polenga Adamu ndi Hava. Anaona kuti Adamu ndi Hava anali okongola kuposa zina zimene Mulungu analenga. Ndipo anadzinena, 'Ndidzapangitsa Adamu ndi Hava kuda Mulungu, monga inenso ndikuda Mulungu. Ndidzaononga cilengedwa conse cokongola ca Mulungu mwa kupangitsa anthu kukhala osamvera Mulungu.'
Mulungu adapatsa Adamu ndi Hava munda wokongola kuti iwo akhalemo. M'munda munali mitundu iliyonse ya maluwa ndi mitengo. Munali mbalame zoimba. Ndipo kunali zipatso zokoma. Mulungu anakonda Adamu ndi Hava. Ndipo anafuna kuti Adamu ndi Hava azimkonda. Anafuna kuti iwo azimuonetsa kuti amkonda. Kotero anati kwa Adamu ndi Hava, 'Muloledwa kudya zipatso zonse zimene mufuna. Koma muli mtengo umodzi m'munda umene simuloledwa kudya'. Mwa kumvera Mulungu ndi kusiya mtengo umenewo, iwo anaonetsa kuti amkonda. Mulungu anatinso, 'Ukadya cipatso ca mtengowo, mudzafa ndithu.'
Satana anamva zimene Mulungu ananena. Kenaka anapita kulankhula ndi Hava. Anati kwa Hava, 'Simudzafa mukadya mtengowo. M'malo mwa kufa mudzakhala monga Mulungu. Mudzadziwa zabwino ndi zoipa.'
Hava anamvera za Satana. Anamkhulupirira. Anayang'ana mtengo ndipo anaganiza kuti cipatso cioneka bwino kucidya. Anaganiza za zimene Satana adanena, kuti adzakhala monga Mulungu atadya cipatso. Anaiwala kuti anali kale wofanana ndi Mulungu; Mulungu adalenga Adamu ndi Hava okongola ndi abwino m'cifanizo cace. Hava anaiwala zimenezo. Anaganiza kuti atadya cipatsoco adzakhala okongola kwambiri kopambana momwe anali.
Kenaka anatenga zipatso zina nadya. Iye anadya cipatso cimene Mulungu anamletsa kudya. Anapatsa zina za Adamu ndipo iye anadyanso.
Kotero Adamu ndi Hava anacita cimene Satana anafuna kuti iwo acite. Ndipo anacita cimene iwo anafuna kucita, m'malo mwa kucita cimene Mulungu anafuna.
Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu. Iwo anakhala ocimwa. M'malo mwa kufanana ndi Mulungu anafanana ndi Satana. M'malo mwa kukonda Mulungu anayamba kumva mantha ndiponso kumuda Mulungu.
Ooo, tsiku ilo linali tsiko lacisoni kwambiri. Cimwemwe conse anacoka m'mitima ya Adamu ndi Hava. Ndipo pa tsiku ilo zinthu zosakondweretsa ndi zoipa zinayamba.
Satana anakondwera. Koma Adamu ndi Hava sanakondwere. Ndipo Mulungu sanakondwere.

**Kukambirana**
1. Kodi Satana ndiye yani?
2. Chimo ndi kusamvera Mulungu. Patsani zitsanzo za kusamvera Mulungu.
3. Kodi Adamu ndi Hava anakondadi Mulungu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wamkulu ndi woyera, Tidzicepetsa cifukwa tikumva manyazi. Adamu ndi Hava sanakumvereni. Ndipo ifenso sitikumverani nthawi zambiri. Nthawi zambiri tiiwala Inu. Nthawi zambiri tiganiza kuti maganizo athu ndiwo abwino oposa maganizo anu. Conde, mutikhululukire kuti tikhale pafupi ndi Inu. Mutipangitse kukhala okondwera mwa Yesu, Mwana wanu. Amen.

## 5. Zimene zinacitika kwa Adamu ndi Hava

*Ndipo macimo anu abisa nkhope yace kwa inu – Yesaya 59.2*

**Kuwerenga**
Genesis 3.7-10

**Malongosoledwe**
Kodi mukumbukira cimene Mulungu ananena kwa Adamu ndi Hava za mtengo m'munda? Kodi mukumbukira cimene Iye ananena kuti cidzacitika ngati iwo adya cipatso ca mtengowo? Anati, 'Tsiku limene mudzadya mtengo wadziwitsa zabwino ndi zoipa mudzafa ndithu.'
Kodi Adamu ndi Hava anafa pa tsiku lomwelo?
Matupi ao sanafe pa tsiku ilo. M'njira iyo Adamu ndi Hava anakhala moyo zaka zina zambiri. Koma anafa m'njira ina.
Analekanitsidwa ndi Mulungu.
Tifunika kukhala ndi Mulungu kuti ndife okondwera. Kukhala kopanda Mulungu ndi kulekanitsidwa ndi Mulungu ndiko koipa kwambiri. Ndipo ico ndi cimene cinacitika kwa Adamu ndi Hava.
Mulungu ankabwera ku munda. Ankayenda ndi Adamu ndi Hava nalankhula nao.
Kucokera pa nthawi yakudya cipatso coletsedwa ndi Mulungu, Adamu ndi Hava anamva mantha ndi Mulungu. Ndipo anamvanso manyazi. Anathawa. Anayesa kubisala. Anayesa kubisala kwa Mulungu, koma kulibe munthu amene angacite tero!
Patapita nthawi Mulungu anabwera ku munda. Anaitana, 'Adamu, uli kuti?'
Adamu anadziwa kuti sangabisale kwa Mulungu. Mulungu aona zonse. Adamu anacoka ku malo obisalako. Anauza Mulungu kuti anamva mantha.
Mulungu anati, 'Kodi wacita ciani?'
Pamenepo Adamu anayenera kuuza Mulungu zimene adacita. Ooo, anamva manyazi ndi mantha kwambiri!
Mulungu ndiye woyera kwambiri. Alibe chimo lirilonse. Chimo litipangitsa kukhala osayera. Ndipo litilekanitsa ndi Mulungu. Ngati si ndife oyera sitikhoza kukhala pafupi ndi Mulungu.
Adamu ndi Hava anadziwa kuti adacimwa. Anamcitira Mulungu mwano. Cifukwa cace anaopa. Anadziwa kuti Mulungu ndiye woyera. Anadziwa kuti ayenera kulangidwa cifukwa ca uchimo wao.
Mulungu anauza Adamu ndi Hava kuti zowawa ndi matenda zidzabwera kucokera ku nthawi iyo. Anawauza kuti matupi ao adzafa patapita nthawi. Anawacotsa m'munda wokongola. Sanayenerebe kukhalamo. Munda unali wokongola kwambiri kuti anthu ocimwa angakhalemo. Mulungu anawauza kuti iwo afunika kugwira nchito molimbika kuti akhale ndi moyo. Ndipo Mulungu sanabwerenso kuyenda ndi kulankhula nao, monga ankacita kale.

Zinthu zambiri zobvutitsa zinayamba pa tsiku limene Adamu ndi Hava anacimwa. Coipa coposa cinali kuti iwo analekanitsidwa ndi Mulungu ndipo anamva manthu ndi Iye.
Kucokera ku tsiku ilo anthu amamva mantha ndi Mulungu. Pamene tikumbukira kuti Mulungu ndiye woyera kwambiri ndiponso kuti ndife ocimwa kwambiri tikumva mantha.
Koma pa tsiku limenelo Mulungu analonjeza Adamu ndi Hava kuti tsiku lina zonse zidzakhalanso bwino. Analonjeza Mpulumutsi womwe adzacotsa macimo ndi kutibweretsanso kwa Mulungu, kuti sitiyenerabe kumva mantha.
Mulungu atikondabe kwambiri!

**Kukambirana**
1. Ndi cifukwa ciani Adamu ndi Hava anacita mantha ndi Mulungu?
2. Kodi iwo anayesa kucita ciani?
3. Kodi iwo anafa m'njira yotani pa tsiku limenelo?
4. Chulani zinthu zina zosayenera zimene zinacitika.
5. Cifukwa ca Yesu tingakhale pafupi ndi Mulungu. Kodi ici citanthauza ciani?
6. Kodi tiyenera kucita ciani titacimwira Mulungu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu woyera, Tiri ndi mitima yocimwa. Mutithandize kucita zabwino. Pamene Satana afuna kuticimwitsa, mutipatse mphamvu yokanira zoipa. Mutiphunzitse masiku onse kuti tikulondolani moonadi. Mutikhululukire macimo athu onse m'dzina la Yesu. Amen.

## 6. Citanthauzo ca kukhala wocimwa

*Tonse tasocera ngati nkhosa – Yesaya 53.6*

**Kuwerenga**
1 Yohane 1.8-10

**Malongosoledwe**
Kodi musamvera nthawi zina?
Anyamata ndi atsikana onse samvera nthawi zina. Ngakhale tiana tankhanda tokondedwa sitimvera nthawi zina. Ngakhale akulu samveranso.
Kodi kusamvera ndi koipa?
Inde, kusamvera ndi koipa, cifukwa ndiko chimo, chimo kwa Mulungu.
Kodi mudziwa citanthauzo ca ico?
Pamene tacimwa talephera kucita cimene Mulungu afuna kuti tizicita. Mulungu anatilenga. Ndife ace. Tiyenera kucita zimene atiuza kuti tizicita cabe. Tiyenera kukhala monga Iye afuna kuti tizikhala cabe. Tiyenera kumkonda ndi kumumvera nthawi zonse. Tiyenera kumkonda cifukwa Iye ndiye wodabwitsa ndiponso cifukwa atikonda.
Pamene Adamu ndi Hava anacimwira Mulungu (kusamvera ndi kudya cipatso coletsedwa) chimo linabwera naononga dziko lonse lapansi lokongola la Mulungu. Linaononganso Adamu ndi Hava. Adamu ndi Hava anakhala ocimwa. Analoledwa Satana kulowa m'mitima yao ndipo kucokera ku nthawi iyo sanakwaniritse kumvera Mulungu m'njira yoyenera.
Pamene Adamu ndi Hava anakhala ndi ana, ana ao naonso ndi ocimwa. Makanda onse abadwa ndi uchimo m'mitima yao. Cifukwa cace ngakhale ana akhanda samvera nthawi zina. Ico ndi cacisoni, iai?
Tikacita cimene Mulungu atiletsa, tacimwa.
Pamene siticita cimene Mulungu afuna kuti tizicita, tacimwa.
Ooo, inde, timacimwira Mulungu kwambiri.
Nthawi zambiri sitifuna kumvera Mulungu. Tifuna kusamvera.
Zoona, Mulungu anganaleke kukonda Adamu ndi Hava pamene iwo anamcimwira, iai? Zoona sangatikonde pakuti ndife ocimwa, iai?
Ooo, Mulungu ndiye wabwino ndi wacifundo kwambiri! Sanaleke kukonda Adamu ndi Hava. Ngakhale pamene anati kuti iwo adzakhala ndi zowawa, ululu wa m'mtima ndi zobvuta, Iye anawakonda.
Mulungu anasamalira Adamu ndi Hava. Kodi mukumbukira kuti anawalonjeza cinthu codabwitsa? Analonjeza kuti tsiku lina adzatuma Mpulumutsi amene adzacotsa uchimo.
Mulungu safuna anyamata ndi atsikana kukhala osamvera. Koma saleka kukukondani pamene musamvera. Sakonda zosamvera zimene mwacita. Akuda uchimo, koma akukondani. Akukondani tero kuti anatuma Mpulumutso wolonjezedwa. Anatuma Yesu kuti acotse macimo anu ndi anga.
Ooo, tiyenera kukonda Mulungu kwambiri-mbiri. Tiyenera kumkonda kwambiri tero kuti sitifuna kucimwa. Mulungu ndi wabwino kwambiri kwa ife!

**Kukambirana**
1. Kodi ocimwa ndiwo anthu otani?
2. Kodi chimo loyamba la Adamu ndi Hava linali lotani?
3. Aliyense pa dziko lapansi abadwa ndi mtima wocimwa. Ndi zoona kapena bodza?
4. Kodi Mulungu analeka kutikonda?
5. Yesu anafa pa mtanda kukhululukira macimo a anthu ace. Kodi ndinu wace?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wacikondi, ndife okondwera kuti simunaleke kukonda dziko lapanso locimwa. Ndinu wacisomo kwambiri. Mutikhululukire kusamvera kwathu. Mutithandize kukukondani. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu Mpulumutsi. Amen.

## 7. Zifukwa zake za kulangidwa kwa uchimo

*Pakuti mphoto yace ya uchimo ndi imfa – Aroma 6.23*

**Kuwerenga**
Genesis 8.6-16

**Malongosoledwe**
Kodi amai anu akupatsani cilango nthawi zina? Kapena atate anu akulangani?
Ndi cifukwa ciani amai kapena atate anu apatsa cilango? Pamene musamvera mufunika kulangidwa. Amai amapatsa cilango cifukwa ico ndi coyenera. Kusamvera konse kufunika kulandira cilango.
Ndipo kuli cifukwa cina. Amai kapena atate akupatsani cilango kuti mukhale olungama. Cilango cimatithandiza ife kuleka zoipa, si tero kodi? Kotero cilango ndi cabwino. Cilango ndi cabwinonso ku anthu akulu. Cilango cimatithandiza kuphunzira kukhala umoyo wosangalatsa Mulungu.
Mulungu ndiye woyera. Kodi mukumbukira kuti angelo amamlemekeza mwa kuimba 'Woyera, woyera, woyera'? Mulungu alibe chimo lirilonse. Iye ndiye woyera ndi wacilungamo. Afuna kuti ifenso tizikhala woyera ndi olungama. Afuna kuti tifanana naye.
Mulungu sangatilole kucita coipa kopanda kutilanga, cifukwa Iye ndiye woyera kwambiri. Tikamcimwira tiyenera kulandira cilango.
Pamene sitimvera atate athu kapena amai athu tawacimwira. Koma tikacita tero tacimwiranso Mulungu, cifukwa Mulungu auza ana kuti ayenera kumvera makolo ao. Chimo ndi loipa kwambiri-mbiri.
Uchimo unabwera pa dziko lapansi pamene Adamu ndi Hava anacimwa. Kodi mukumbukira zimene zinacitika? Kucokera pa nthawi iyo uchimo unakula koposa. Posacedwa kunali anthu ambiri pa dziko lapansi ndipo iwo anali oipa kwambiri.
Mulungu anali wacifundo kwa iwo. Sanawapatse cilango nthawi yomweyo. Anayembekeza nthawi yaitali. Anafuna anthu kubwereranso kwa Iye ndi kumtumikiranso.
Koma tsiku lina, pamene Mulungu anayang'ana pa dziko lapansi, anaona banja limodzi cabe limene anayesadi kukhala olungama ndi kumtumikira. Ilo linali banja la Nowa. Anthu ena onse anali oipa kwambiri. Anapanga dziko lokongola la Mulungu kukhala malo oipa.
Mulungu anati, 'Ndidzaononga anthu onse a pa dziko lapansi. Ndidzacotsa zoipa zao zonse.'
Mulungu anauza kuti adzatumiza mvula lalikulu kudzadza dziko lonse lapansi ndi madzi. Ndipo anauza Nowa kupanga combo, ndico cingalawa cacikulu. Ico cinayenera kuoneka monga nyumba. Cinayenera kukhala monga nyumba ya tsanja ndiponso kukhala ndi citseko ndi dzenera.
Nowa ndi ana ake anagwira nchito molimba popanga combo. Ndipo anauza anzao za cigumula. Koma kunalibe amene anakhulupirira kuti cigumula cidzabweradi.
Anatsiriza kupanga combo. Nowa ndi banja lake analowamo, pamodzi ndi nyama zonse zimene Mulungu anafuna kupulumutsa. Kenaka Mulungu anatumiza cigumula. Madzi anali ponseponse pa dziko lapansi. Anthu oipa onse anafa. Iwo okhala m'combo cabe anapulumuka.
Ico cinali cilango coipa kwambiri.
Koma Baibulo likamba kuti chimo lirilonse liyenera kulangidwa ndi cilango coipa: macimo anu ndiponso macimo anga ayenera kulangidwa. Baibulo likamba kuti ocimwa onse amene sabwereranso kwa Mulungu adzatayika ku nthawi zosatha.

**Kukambirana**
1. Ndi cifukwa ciani cilango ndi coyenera ndi cabwino?
2. Kodi Mulungu angatipatse cilango cotani?
3. Mulungu anapulumutsa banja la Nowa mwa cisomo. Kodi cisomo ndi ciani?
4. Ndi cifukwa ciani anthu osalapa ayenera kukhala ku Gehena?
5. Yesu anafa pa mtanda kusenza cilango ca uchimo. Kodi anasenzanso cilango ca macimo anu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Inu ndinu woyeradi. Mulibe chimo lirilonse. Koma ife tiri ndi macimo ambiri cifukwa ca mitima yathu yocimwa. Tiyenera kulangidwa cifukwa ca uchimo wathu. Ngakhale ngati tiyesa kusiya uchimo, tipeza uchimo m'mitima yathu. M'Baibulo tiwerenga kuti Yesu akwaniritsa kuyeretsa ku macimo. Mutiyeretsenso masiku onse kuti tizikhala olungama pa maso panu. M'dzina la Yesu tikupemphani izi, mwa cisomo. Amen.